
**MISSIONARY MESSAGE OF THE BIBLE (NYANJA)**
**PUBLISHED BY THE BAPTIST PUBLISHING HOUSE**
**PRINTED BY THE BAPTIST PRINTING MINISTRY**
**BOX 1995, LUSAKA, ZAMBIA**

4104

# KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA



**NDI PAULA KILPATRICK**

W221
NYA

MISSIONARY MESSAGE OF THE BIBLE
(NYANJA)

FIRST PUBLISHED
OCTOBER 1, 1978

BY THE
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

PRINTED BY
THE BAPTIST PRINTING MINISTRY
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

SABATA LACISANU NDI CITATU: Yesu ndi Ahelene

Tsiku 1: Mateyu 8.5-13
Tsiku 2: Yohane 4.1-43
Tsiku 3: Mateyu 15.21-28
Tsiku 4: Afilipi 2.9-11
Tsiku 5: Yohane 12.20-32
Tsiku 6: Macitidwe 11.17-18

SABATA LACISANU NDI CINAI: Imfa ndi kuuka kwa Yesu.

Tsiku 1: Masalmo 22
Tsiku 2: Marko 15-16
Tsiku 3: Mateyu 27.27-54
Tsiku 4: Luka 24.13-32
Tsiku 5: Yohane 19.17-37
Tsiku 6: Yohane 20.1-10

SABATA LA KHUMI: Ziphunzitso zomalizira za Yesu.

Tsiku 1: Mateyu 24.14
Tsiku 2: Luka 24.44-49
Tsiku 3: Yohane 20.19-23; 26-29
Tsiku 4: Yohane 21.15-17
Tsiku 5: Mateyu 28.19-20
Tsiku 6: Macitidwe 1.6-8

SABATA LA KHUMI NDI LIMODZI: Mzimu Woyera umpatsa mphamvu ya kucitira umboni.

Tsiku 1: Aefeso 3.14-20
Tsiku 2: Macitidwe 2.1-4
Tsiku 3: Yohane 14.15-24
Tsiku 4: Yohane 16.5-15
Tsiku 5: Macitidwe 10.34-43
Tsiku 6: Macitidwe 10.44-48

SABATA LACISANU: Colinga ca Mulungu cinabvumbulutsidwa kwa Aneneri.

Tsiku 1: Yona 1-4
Tsiku 2: Yoswa 9
Tsiku 3: Masalmo 47
Tsiku 4: Masalmo 117
Tsiku 5: Masalmo 67
Tsiku 6: Masalmo 96

SABATA LACISANU NDI LIMODZI: Yesu akwanilitsa lonjezo la Mulungu.

Tsiku 1: Afilipi 2.5-8
Tsiku 2: Aroma 5.12-25
Tsiku 3: 2 Akorinto 5.21
Tsiku 4: Mateyu 16.24-25
Tsiku 5: Agalatiya 2.15-16
Tsiku 6: 1 Petro 2.4-10

SABATA LACISANU NDI CIWIRI: Yesu ndi Ayuda

Tsiku 1: Luka 14.16-24
Tsiku 2: Luka 10.25-37
Tsiku 3: Luka 15
Tsiku 4: Mateyu 10.5
Tsiku 5: Mateyu 15.21-28
Tsiku 6: Aroma 9.30-33



KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M BUKU LOPATULIKA

MUTU TSAMBA


1. PANGANO LA MULUNGU....................1

2. MULUNGU ASANKHA ABRAHAMU..............4

3. MOSE ATSOGOLERA ANTHU A MULUNGU.......7

4. ENA AMENE ANATSATIRA MULUNGU.........10

5. COLINGA CA MULUNGU CINABVUMBULUTSIDWA KWA ANENERI..........................13

6. YESU ALI KUKWANILITSA LONJEZO LA MULUNGU.............................16

7. YESU NDI AYUDA......................19

8. YESU NDI AHELENE....................22

9. IMFA NDI KUUKA KWA YESU..............25

10. ZIPHUNZITSO ZOTSILIZIRA ZA YESU .....27

11. MZIMU WOYERA UMAPATSA MPHAMVU YA KUCITIRA UMBONI......................30

KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

MUTU 1

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: PANGANO LA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Aefeso 3:1-13

**MAU** APAMTIMA: *"Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife."*
*Aroma 5.8*

MTSOGOLERI:

"Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi." (Genesis 1.1). Ndime yoyamba M'buku Lopatulika imayankha funso loyenera lomwe anthu onse amafunsa. Anthu onse amafunsa, "Kodi ndani anacita ici? Buku Lopatulika linena kuti, "Mulungu anacita ici. "Buku Lopatulika linena kuti Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. Ndipo mbali yotsalira M'Buku Lopatulika linena za cifukwa comwe Mulungu adalenga dziko lapansi.

Mulungu ali ndi colinga mzonse zomwe acita. Mukhoza kudziwa colinga cace pa anthu onse ndi ca inu pakuphunzira Buku Lopatulika.

GAWO LOYAMBA: KUFUNIKA KWA PANGANO

Mitu khumi ndi umodzi wa buku la Genesis itiuza za kalengedwe ka dziko lapansi ndi munthu. Mulungu adalenga munthu motero kuti akhale mciyanjano ndi Mulungu. Pamene munthu anacimwa naswa ciyanjano ndi Mulungu,



SABATA LOYAMBA: Pangano la Mulungu

| | |
|---|---|
| Tsiku 1: | Yohane 3.16-21 |
| Tsiku 2: | Yohane 1.1-18 |
| Tsiku 3: | 1 Yohane 4.7-10 |
| Tsiku 4: | Aefeso 3.1-13 |
| Tsiku 5: | Marko 12.28-34 |
| Tsiku 6: | 1 Yohane 5.1-5 |

SABATA LACIWIRI: Mulungu asankha Abrahamu

| | |
|---|---|
| Tsiku 1: | Macitidwe 7.2-8 |
| Tsiku 2: | Aroma 4.1-5 |
| Tsiku 3: | Yakobo 2.18-24 |
| Tsiku 4: | Genesis 22.15-18 |
| Tsiku 5: | Ahebri 11.8-22 |
| Tsiku 6: | Agalatiya 3.6-9 |

SABATA LACITATU: Mose atsogolera anthu a Mulungu

| | |
|---|---|
| Tsiku 1: | Eksodo 19.1-8 |
| Tsiku 2: | Ahebri 11.23-29 |
| Tsiku 3: | Numeri 14 |
| Tsiku 4: | Eksodo 3.1-12 |
| Tsiku 5: | Macitidwe 7.17-34 |
| Tsiku 6: | Macitidwe 7.35-43 |

SABATA LACINAI: Ena amene anatsatira Mulungu

| | |
|---|---|
| Tsiku 1: | Numeri 10.29-32 |
| Tsiku 2: | Numeri 22-24 |
| Tsiku 3: | Yoswa 2.1-21<br>Yoswa 6.22-25 |
| Tsiku 4: | Rute 1-4 |
| Tsiku 5: | 2 Mafumu 5.1-14 |
| Tsiku 6: | Eksodo 18.10-12 |

uli kutsogolera anthu kugawirana nkhani yabwino ya Yesu ndi anthu onse. Anthu ambiri amvera nkhani yabwino kamba kakuti Mzimu Woyera analankhula kwa Akristu ndi kuwatumiza monga m'mene anatumira mtumwi Paulo ku malo ena komwe sanamveke za nkhani yabwino.

MTSOGOLERI:

Colinga ca Mulungu sicinasinthe. Ciri colinga ca Mulungu kwa anthu onse a mdziko lapansi kuti amdziwe monga Mulungu mmodzi yekha woona. Kucokera pa nthawi yomwe Yesu Kristu anali pa dziko lapansi, anthu a Mulungu osankhidwa amene adzakwanilitsa lonjezo latsopano ndi anthu ochedwa Akristu. Aliyense wa ife amene analandila Yesu m'mitima yathu ndipo ali ndi moyo ali ndi nchito imodziyo yonse yomwe inapatsidwa kwa ana a Abrahamu. Munthu aliyense ayenera kumvera Mulungu. Munthu aliyense akhoza kukhala ndi dalitso kwa anthu onse a mdziko lapansi pamene aonetsa anthu Yesu.



Mulungu anayamba kufuna funa njira yomwe munthu angabwelerenso kwa iye. Buku Lopatulika litiuza m'mene Mulungu abvumbulutsira njira yace. M'masiku a Mcipangano Cakale Mulungu anabvumbulutsa pangano lace kapena njira yace kupyolera mwa aneneri ndi anthu ena oyenera. Mu Cipangano Catsopano Mulungu anabvumbulutsa njira yace kupyolera mwa Mwana wace Yesu Kristu.

GAWO LACIWIRI: PANGANO LINABVUMBULUTSIDWA

Pamene Yesu anabwera mdziko lapansi kudzakhala monga munthu, anaonetsa njira ya Mulungu kwa munthu moyenera. Njira ya Mulungu kwa munthu yakhala yabwino kwa nthawi zonse. Pamene Yesu anabwera nafa pamtanda kamba ka macimo a munthu, anaonetsa mmene cikondi cace cacikuru ciliri kwa munthu. "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife." (Aroma 5.8)

GAWO LACITATU: PANGANO LINAGAWIDWA

Pamene Yesu Kristu anafa pamtanda, anauka kucokera mmanda, ndipo anapita kumwamba, ciri conse comwe munthu anafuna kuti akhale mciyanjano ndi Mulungu cinacitika. Nchito yonse yacipulumutso ca munthu inacitika. Tsopano munthu akanayankha Mulungu mwa cikhulupiliro ndipo akanalandira cipulumutso. Tsopano anthu onse akhoza kubwera kwa Mulungu

Mulungu sanakonze cabe njira yakuti munthu alandile Yesu Kristu monga Mpulumutsi wace. Ndi njira yace yakutinso iwo amene akhulupilira mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi

ayenera kugawirako njirayo ya cipulumutso. kwa anthu onse.

MTSOGOLERI:

Buku Lopatulika litiuza kuti Mulungu ali ndi colinga pa munthu. Colinga cace ndicakuti, munthu akhoza kukhala mciyanjano ndi iye kupyolera mwa Mwana wace Yesu Kristu amene analankhula kuti, "Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine." (Yohane 14.6)



Mulungu unali wosiyana ndi womwe anali kuphunzira kucokera pomwe anali mwana. Pamene Petro anatsimikizidwa ku zomwe Mulungu anafuna kuti iye acite, anatsatira zomwe Mulungu anafuna kuti iye acite.

Pamene analalikira ku nyumba ya Korneliyo, nyumba yonse inalandira Yesu Kristu monga Ambuye ndi Mpulumutsi wawo, Petro anamvetsetsa uthenga wa Mulungu kwa iye. "Ndipo Petro anatsegula pakamwa pace, nati, Zoona ndizindikira kuti Mulungu alibe tsankhu, Koma m'mitundu yonse, wakumuopa Iye ndi wakucita cilungamo alandiridwa naye." (Macitidwe 10.34-35). Petro anatenga uthenga wabwino kwa Ayuda ndi Ahelene.

GAWO LACITATU: DZIKO LONSE LIKUMVA NKHANI YABWINO

Mzimu Woyera anatsogolera Akristu oyamba mmalo onse a dziko lapansi. Pamene Akristu anayenda mmalo osiyana siyana, anauza onse amene anali kumvera za Yesu ndi imfa ndi kuuka kwace. Anthu ambiri anakhulupilira. Ophunzira anakhala okhulupilira kwa Yesu mnthawi ya mazunzo.

Mtumwi Paulo ataona Yesu pa mseu wa ku Damasiko anali munthu woyenera kutenga nkhani yabwino kwa Ahelene. M'maloto Paulo anaona munthu ali kumuuza kucokera ku Mesodoniya kuti abwere ku dziko lace ndi kulalikira nkhani yabwino. Pomwe asanafe mu Aroma, Paulo anapanga mipingo yambiri yomwe inali ndi okhulupirika a ci Yuda ndi Ahelene.

Kupyolera mzaka Mzimu Woyera wakhala

panganó la Mulungu la kubweretsa anthu onse a mdziko lapansi kwa iye. Ophunzira a Yesu anaona cibvumbulutso conse ca Mulungu kupyolera mwa Yesu. Nchito ya Mesiya inatha. Tsono kupyolera mphamvu ya Mzimu Woyera guru laling'ono la ophunzira ankauza anthu onse nkhani yabwino mdziko lonse.

GAWO LOYAMBA: AYUDA AKUMVA NKHANI YABWINO PA PENTEKOSTE

Cimodzi ca zizindikilo kuti Mzimu Woyera anadza mwa ophunzira pa Pentekoste cinali cakulankhula kwa ophunzira mzilankhulidwe 15 zosiyana siyana. Anacitira umboni Yesu kwa munthu aliyense mcilankhulidwe cace mwini kwa iwo amene anabwera kucokera ku maiko ena a mdziko lapansi ku phwando la Pentekoste.

Pamene Petro analalikira kwa anthu, munthu aliyense amene anali kumvera iye anamva zomwe Petro anali kunena. Anthu opitilira pa ciwerengelo ca 3,000 anakhala otsatira a Yesu pa tsikulo la Pentekoste.

GAWO LACIWIRI: AHELENE AKUMVA NKHANI YABWINC

Korneliyo anali kenturiyo wa ci Roma. Sanali Myuda, koma anali munthu amene anapembedza Mulungu. Pamene Mulungu analankhula kwa Korneliyo, Korneliyo anamvera ku zisonyezo za Mulungu natuma anthu ena kukaitana Petro.

Pamene Mulungu ahalankhula kwa Petro mu ciloto, Petro sanali osimikizidwa ku zomwe Mulungu anamuonetsa. Uthenga wa



MUTU 2

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: MULUNGU ASANKHA ABRAHAMU

MAU A MULUNGU: Macitidwe 7.2-8

MAU APAMTIMA: *"Ndipo anakhulupirira Yehova, ndipo kunayesedwa kwa iye cilungamo."*
*Genesis 15.6*

MTSOGOLERI:

Mitu khumi ndi umodzi yoyamba ya Genesis itiuza kuti munthu anayipa pomwe cimo linalowa mdziko lapansi. Nthawi ina kunali cabe munthu mmodzi wolungama yemwe anali mdziko lapansi. Munthu uyu anali Nowa. Mulungu anaononga dziko lonse kucotserapo Nowa, banja lace ndi nyama ili onse mcombo; koma cigumula citatha banja la Nowa linayambanso kukhala muucimo mdziko lapansi.

Mulungu amadziwa kuti kunali cabe njira imodzi yomwe inkapambana cimo motero kuti munthu akhale mciyanjano ndi Mulungu.

GAWO LOYAMBA:LONJEZO KWA ABRAHAMU

Mulungu anayamba pangano lace pakusankha munthu wochedwa Abrahamu. Abrahamu sanasankhidwe kamba kakuti Mulungu anamkonda kopambana anthu ena mdziko lapansi. Abrahamu sanasankhidwe kamba kakuti anali munthu wolungama monga Nowa. Buku Lopatulika

silitiuza ndi cifukwa ninji anasankha Abrahamu. Mulungu anauza Abrahamu kucita cinthu cina ndipo Mulungu anapereka lonjezo kwa Abrahamu. Abrahamu anakhulupirira Mulungu. Mulungu anakhoza kugwiritsa nchito Abrahamu mpangano lace cifukwa Abrahamu anakhulupilira Mulungu.

Genesis 12:1-3 tiwerenga zomwe Mulungu analankhula kwa Abrahamu. Mulungu anauza Abrahamu kuti acoke mdziko lace ndi kupita ku dziko lomwe Mulungu ankamusonyeza. Mulungu anati, "Ngati udzacita ici, ndidzakuyesa iwe mtundu waukuru. Ndidzakudalitsa ndi kukhala iwe mdalitso kwa anthu onse a mdziko lapansi."

GAWO LACIWIRI: LONJEZO KWA ISAKE

Mulungu anayesa cikhulupiliro ca Abrahamu pamene anamulamulira kuti akapereke nsembe mwana wace mmodzi yekha yemwe anali naye. Pamene Abrahamu anakonzeka kumvera Mulungu, Mulungu anapereka nsembe ina. M'buku la Ahebri 11.19 mau a Mulungu akuti Abrahamu anakhulupilira kuti ngati Isake anafa, Mulungu ankamubweretsanso kwa akufa.

Abrahamu anaphunzitsa Isake zomwe Mulungu anamubvumbulutsira. Nthawi ya nsembe itapita, Mulungu anakumbutsanso Abrahamu lonjezo lace, Koma pamene Isake anakula, Mulungu mwini analankhula kwa Isake nalankhulanso za lonjezo kwa iye. (Genesis 26.2-5).

GAWO LACITATU: LONJEZO KWA YAKOBO

Isake anali ndi ana a mapasa, Yakobo ndi Esau. Mulungu anasankha mwana wa mng'ono Yakobo kuti apitirire ndi lonjezo.



kuti ndiwo amene adzatenga uthenga wace wa cipulumutso ku dziko lonse lapansi. Anawauzanso kuti sadzakhala okha. Akuti adzakhala ndi iwo pamene ali kupita ku malo awa ndi awa kuuza aliyense za Yesu Kristu.

**MUTU 11**

**COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA**

**COLINGA CA LERO: MZIMU WOYERA UMAPATSA MPHAMVU YA KUCITIRA UMBONI**

**MAU A MULUNGU: Macitidwe 2.1-12,38-39**

**MAU APAMTIMA:** ***"Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko."***

***Macitidwe 1.8***

**MTSOGOLERI:**

**Yesu anauza ophunzira ace kuti adikhire mu Yerusalemu kufikira atalandila mphamvu ya Mzimu Woyera yemwe anafunika kulandila motero kuti akhale mboni zace. Ophunzira anali pamodzi ali kupemphera pa nthawi ya Pentekoste pamene Mzimu Woyera anadza kuwapatsa mphamvu.**

**Pamene ophunzira analandila mphamvu ya Mzimu Woyera, anali okonzeka tsopano kukwanilitsa**

Mu Yohane 20.19-23 Yesu anati kwa ophunzira ace, "Mtendere ukhale ndi inu, monga Atate wanditurna Ine, Inenso nditurna inu." Yesu anali kutumiza ophunzira ace mdziko kuti acite nchito yaikuru. Anali kuwatumiza kuti atenge Uthenga wace wa kutembenuka ndi cipulumutso, ku dziko lonse lapansi. Kaciwirinso ali kuwapatsa mphamvu ya Mzimu Woyera kuti awatsogolere pamene ali kucita nchito yace.

Mu Yohane 21.15-17 Yesu anali kulankhula kwa Petro za nchito yace mu ufumu wa Mulungu anafunsa Petro katatu ngati ndithudi anamkonda. Nthawi iri yonse Petro anati inde. Yesu anamusonyezanso nthawi iri yonse ponena kuti "Dyetsa nkhosa zanga." Yesu anali kuuza Petro kusamala iwo amene anafera kuti awapulumutse. Mu ndime ya 19 Yesu anati kwa Petro "Nditsate ine." Mau amene analankhula kwa Petro ali kulankhulanso kwa okhulupirika aliyense lero.

GAWO LACITATU: MATEYU 28.16-20

Lamulo lalikuru pa za ulaliki liri lolembedwa kupambana kamodzi m'mabuku anai (Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane). Yesu analankhula kwa ophunzira ace kumbari kwa Galileya. Anauza ophunzira ace kutenga uthenga wace ku dziko lonse lapansi ndi kupanga ophunzira ena pamene anali kuyenda. Sanawapatse cabe lamulo lakupita mdziko lapansi, koma anawauza kuti adzakhala nawo kwa nthawi zonse pamene anali kupita.

MTSOGOLERI:

Mndime zonse izi Yesu ali kuuza ophunzira



Tanthauzo la dzina lakuti Yakobo ndi lakuti "Wonamiza." Esau anagulitsa ukuru wace pa za ukuru wa kubadwa kwa Yakobo ndi cakudya. Tsono Yakobo ananamiza Esau pa za madalitso ace. Yakobo anali kufuna madalitso a moyo, koma sanadziwe njira yoyenera kutengelamo madalitsowo. Mulungu anaona cinthu cina mwa Yakobo comwe ankagwiritsa nchito.

Pamene Yakobo anathawa mkuru wace Esau, Mulungu analankhula kwa Yakobo m'maloto. Yakobo anayamba kuphunzira kwa Mulungu. Coyamba anaphunzitsa kuti Mulungu sanali Mulungu wa Isake yekha. Anaphunzira kuti Mulungu ali Mulungu wa anthu onse. Mulungu anayamba kupanga Yakobo kukhala mwamuna amene angagwiritse nchito. Patapita zaka zambiri dzina la Yakobo linasintha kukhala Israyeli kutanthauza kuti, "Iye amene amatsala ndi Mulungu." (Genesis 35.10).

MTSOGOLERI:

Abrahamu, Isake ndi Yakobo anali amuna a cikhulupiliro. Anakhulupilira Mulungu naphunzira kukhala okhulupilika kwa Mulungu. Mphamvu yakuona lonjezo la Mulungu lisamila pa kumvela.

MUTU 3

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: MOSE ATSOGOLERA ANTHU A MULUNGU

MAU A MULUNGU: Macitidwe 7.17-34

MAU APAMTIMA: *"Koma cikhulupiriro ndico cikhazikitso ca zinthu zoyembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka. Pakuti momwemo akulu anacitidwa umboni."* *Ahebri 11:1-2*

MTSOGOLERI:

Mzaka zomwe ana a Israyeli anali kukhala mu Aigupto, mbali yoyamba ya lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu linakwanilitsidwa. Mibadwo ya Abrahamu inacuruka kwambiri ndikuti mfumu Farao inamva mantha kamba ka kucuruka kwa ana a Israyeli. Koma ngakhale kuti kunali cilango ca ukapolo ana a Israyeli anacurukabe mciwerengelo ndi m'mphamvu. Tsono Mulungu anasankha mwamuna ochedwa Mose kuti awatsogolere ku dziko lolonjezedwa ndi kupanga mutundu.

GAWO LOYAMBA: UTUMIKI UFUNA KUMVERA

Patapita miyezi itatu pomwe ana a Israyeli anacoka mu Aigupto, Mulungu analankhula kwa iwo pa Phiri la Sinai. Coyamba Mulungu analankhula kwa Mose. Mulungu anasonyeza Mose mu Eksodo 19.5-6 kuti auze ana a Israyeli kuti ngati adzasunga malumulo a Mulungu, ndiye kuti adzakhala anthu osankhidwa ace



ankayenera kukhala mboni zace ku dziko lonse lapansi.

GAWO LOYAMBA: LUKA 24.44-49

Pa tsiku lomwe anauka kwa akufa nthawi ya mmadzulo, Yesu anaonekera kwa ophunzira ace ndi iwo amene anasonkhana pamodzi ndi iwo. Yesu anawauza kuti ulaliki wonse wa Mcipangano Cakale pa za iye unakwanilitsidwa. Ulalikiwu unali kupezeka mumalamulo a Mose, ndi m'malemba a aneneri ndi Masalmo. Ndi pa nthawi iyi pomwe ophunzira a Yesu anayamba kumvetsetsa za nchito ya Yesu monga Mesiya. Buku la Luka 24:45 linena kuti Yesu anatsegula maganizo a ophunzira ace motero kuti anatha kumva za mau amene analankhula za iye. mu Ndime 46 ndi 47 Yesu ali kutsimikiza mau onse amene analankhula za iye. Yesu anati, "Kwalembedwa kuti Kristu amve zowawa, nauka kwa akufa tsiku lacitatu.

Yesu tsono anasankha otsatira ace amene ayenera kunyamula uthenga wa cikhululukiro ku dziko lonse lapasni. Yesu anadziwa kuti ophunzira ace sankacita nchitoyi mwa mphamvu za iwo okha. Analonjeza kutumiza Mzimu Woyera yemwe ankathandiza iwo ndi mphamvu ya kutenga uthenga kuzungulira dziko lonse lapansi.

GAWO LACIWIRI: YOHANE 20.19-23 ndi Yohane 21.15-17

Yohane amalemba za kuonekera kwa Yesu kwa ophunzira ace mmalo ambiri. Kuonekera kwaceku kwa ciwiri kupezeka mu Yohane 20.19-23 ndi Yohane 21.15-17.

Yesu kwa akufa kuti cikhulupiliro cathu cikhale colungama.

MTSOGOLERI:

Cinthu cacikuru m'mbiri ya dziko lapansi ndi imfa ndi kuuka kwa Yesu. Pamtanda Yesu anakwanilitsa cinthu comwe munthu mwa yekha sankacita. Pamene Mulungu anaukitsa Yesu, cinakhala cotheka kwa munthu aliyense kutengako mbali m'pangano la Mulungu.

MUTU 10

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: ZIPHUNZITSO ZOTSILIZIRA ZA YESU •

MAU A MULUNGU: Macitidwe 1.1-11

MAU APAMTIMA: *"Cifukwa cace Yesu anatinso kwa iwo, Mtendele ukhale ndi inu; monga Atate wanditumu Ine, Inenso nditumu inu."* *Yohane 20.21*

MTSOGOLERI:

Pamene Yesu anaukitsidwa kwa akufa, anaonekera kwa ophunzira ace kwa nthawi zambiri mmasiku makhumi anai pamene asanapite kumwamba. Pamene Yesu Kristu analankhula kwa ophunzira ace, anawauzanso zomwe anafuna iwo kuti acite. Yesu anakumbutsa ophunzira ace kokwanira kasanu atauka kwa akufa kuti



kucokera ku mitundu ya dziko lapansi, ndipo udzakhala mtundu wa ansembe a Mulungu. Ana a Israyeli anabvomekeza mau awa.

GAWO LACIWIRI: LONJEZO KU MTUNDU

Mulungu analankhula kwa ana a Israyeli pa Phiri la Sinai nawapatsa malamulo khumi. Koma angakhale kuti anamva liu la Mulungu sicinacinjirize ana a Israyeli kuswa lamulo loyamba mmasabata atatu,

Mulungu anali wokalipa pamene ana a Israyeli anapanga mwana wa ng'ombe na mpembedza. Mu Eksodo 32.7-8 tiona kuti Mulungu saitana ana a Israyeli "anthu ace" koma "anthu ako" ndi anthu awa.. Ana a Israyeli sanamvelere Mulungu. Sankakhala osamvera Mulungu ndi kukhalabe anthu ace,

GAWO LACITATU: AISRAYELI ALI KUKANA KUKHULUPILIRA LONJEZO LA MULUNGU.

Nkhani ya ana aIsrayeli iri yacisoni kwambiri. Anthu analephera kukhulupilira Mulungu nthawi zambiri. Pamene Mulungu anauza ana a Israyeli kupita ku dziko lolonjezedwa, anakana kupita. Mulungu anawauza kuti anapereka dzikolo kwa iwo comwe anthu anayenera kucita ndi kupita mdzikolo koma anthu anakana kumvera Mulungu.

M'buku la Numeri 14, Mose ali kupempha Mulungu pamene anthu anakana kumvelera Mulungu ndi Mose yemwe. Mulungu ali kuyankha pemphero la Mose kuti adzapulumutsa mtunduwo, koma Mulungu anakana kulola anthu kuti apite

mdzikolo iwo amene anakana. Kwa zaka makhumi anai ana a Israyeli anali kuzungulira mcipululu kufikira Mulungu anakhalanso ndi m'badwo watsopano womwe unkamvera iye.

MTSOGOLERI:

Ana a Israyeli sanamve comwe Mulungu anafuna kuti iwo akhalire. Anthu anadziwa kuti anapembedza Mulungu mmodzi yekha woona ndiponso wa moyo. Ánalephera kumvetsera kuti Mulungu anafuna kuti anthu onse apembedze iye. Anaganiza kuti Mulungu anali wa iwo okha. Sanamvere konse Mulungu mokwanila kuti agwiritsidwe nchito ndi iye kuthandiza anthu ena a mdziko lapansi kuti aphunzire kupembedza iye. Sanakhale konse mu ufumu wa ansembe.



anthu akhalenso ndi mpata wakukhala ndi ciyanjano ndi Mulungu. Monga Mulungu anaperekera nkhosa kwa Abrahamu ya nsembe mmalo mwa Isake anapereka mwana wace mwini Yesu monga nsembe ya anthu onse.

GAWO LACIWIRI: KUZIPEREKA MUNTHU MWINI MONGA NSEMBE PAMTANDA

Yesu anapereka nsembe moyo wace mwini pamtanda cifukwa kunalibe njira ina ya cipulumutso kwa anthu onse. Yesu anabvutitsidwa ndi mayeso kopambana amene munthu aliyense sanaonepo. Anabvutitsidwa ndi mayeso napambana mayesowo pakufa pamtanda.

Timakhala pamodzi ndi Yesu cifukwa pamene anafa anatipanga ife kukhala oyera. Anatipanga ife kukhala mciyanjano ndi Mulungu kamba ka cilungamo cace. Tiri ndi malo mu ufumu wa Mulungu kamba kakuti Yesu anatifera ife.

GAWO LACITATU: MULUNGU APEREKANSO MOYO

Pa tsiku lacitatu Mulungu anaukitsa Yesu kucoka kwa akufa. Yesu anamverera Mulungu. Anakhulupilira kuti Mulungu adzamuukitsa kucokera kwa akufa. Pamene Mulungu anaukitsa Yesu kucokera kwa akufa, mphamvu ya cimo ndi imfa zinapambanidwa. Mantha ndi mlandu mu mtima wa munthu tsopano zikhoza kucotsedwa.

Ciyembekezo cathu ciri mkukhulupirika kwa Yesu Kristu. Comwe Mulungu anacita kwa Yesu, Yesu amacitira kwa anthu amene adzamveradi ndi kukhulupilira. Mulungu anaukitsa

MUTU 9

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: IMFA NDI KUUKA KWA YESU

MAU A MULUNGU: Marko 15.21-39

MAU APAMTIMA: *"Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine."*
*Yohane 14.6*

MTSOGOLERI:

Liu lakuti Kristu ndi liu la ci Helene lomwe litanthauza Mesiya mu ci Ahebri. Mesiya ndi Kristu maina awa atanthauza zodzodzedwa. Ansembe, aneneri ndi mafumu onse anali odzodzedwa. Yesu anali wansembe. mneneri ndi mfumu. Analinso mwana wankhosa wa Mulungu amene ankacotsa macimo a dziko.

GAWO LOYAMBA: YESU, NSEMBE YOKHA

Yesu anati, "Abrahamu anaona tsiku langa." (Yohane 8.56). Lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu linakwanilitsidwa kamba ka imfa ya Yesu pamtanda. Yesu anali nsembe ya Mulungu. Yesu anali nsembe oabe yokha yomwe inkalandilidwa ndi Mulungu.

Yesu sanacimwe. Sankayenera kufa. Anali Mulungu iye mwini. Koma Yesu anazicepetsa monga munthu ndipo anali wokhulupirika kwa Mulungu. Yesu anadziwa kuti cinali cifunilo ca Mulungu kuti iye afe pamtanda motero kuti



MUTU 4

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: ENA AMENE ANATSATIRA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Masalmo 67

MAU APAMTIMA: *M'mwemo mukondane naye mlendo; popeza munali alendo m'dziko la Aigupto."*
*Deuteronomo 10.19*

MTSOGOLERI:

Cipangano Cakale cilankhula za anthu ena amene sanali a Israyeli amene anaphunzira kupembedza Mulungu. Ana a Israyeli anauzidwa ndi Mulungu kukonda mlendo. Ahelene anali kuloledwa kukhala M'yuda ngati anali kukhulupilira mwa Mulungu. Mnthawi zosiyana-siyana m'nkhani ya Mulungu ndi anthu ace, anthu ena amene sanali Ayuda anakhala ali kupembedza Mulungu.

GAWO LOYAMBA: ENA ANASANKHA MULUNGU

Jethro anali mpongozi wa Mose. Anali munthu wa ku Midyani. Jethro anamanga guwa napembedza Mulungu. Anakhulupilira kuti Mulungu anali Mulungu woona. Mose anaitana Hababu mwana wa Jethro, kuyenda ndi ana a Israyeli ndi kugawana ndi ena madalitso a Mulungu.

M'buku la Numeri 22 tiwerenga za Balamu. Sanali wa ci Ahebri, koma anali mneneri wa Mulungu. Pamene ana a Israyeli anayamba

kumenyela dziko lolonjezedwa anathandidzidwa ndi mkazi wochedwa Rehabu. Analandila Yehova monga Mulungu wace ndipo ana a Israyeli analandila iye kukhala mmodzi wa banjalo.

GAWO LACIWIRI: RUTE, MU MOABU.

Nkhani ya Rute iwonetsa kuti Mulungu anafuna anthu ena kukhalako ndi mbali mu pangano lace lakubweretsa anthu onse kwa iye.

Rute anali mtsikana amene anali kukhala mdziko la Moabu. Atafa mwamuna wace, Rute anasankha kupita ndi Naomi, mpongozi wace, pamene anabwerera ku dziko la kwao ku Kanani. Pamene Naomi anauza Rute kuti abwelere ku dziko la kwao mwini, Rute anayankha kuti, "Musandiumirize kuti ndikusiyeni, ndi kubwerera osakutsatani; pakuti kumene mumukako ndimuka inenso, ndi kumene mugonako ndigona inenso; anthu a kwanu ndiwo anthu a kwa inenso ndi Mulungu wanu ndiye Mulungu wanga." (Rute 1:16).

Pambuyo pace Rute anakwatira mlongo wa Naomi wochedwa Boazi. Anali makolo a mfumu Davide. Rute anali kholo la Yesu, Mesiya.

GAWO LACITATU: NAAMANI WA KU SIRIYA

Naamani anali mkuru wa gulu la asilikali a nkhondo a mfumu ya mphamvu ca kumpoto kwa Israyeli. Mtsikana wa mu Israyeli anagulitsidwa mu ukapolo ku mkazi wa Naamani. Pamene mtsikana anadziwa kuti Naamani anali ndi makhate, anauza ambuye wace za mneneri Elisa mdziko la Israyeli.

Naamani anapita ku dziko la Israyeli



Yesu anauza mkazi kuti nthawi idzabwera pamene anthu onse adzapembedza Mulungu mu Mzimu ndi Mcoonadi. Yesu anabvomera ku mkazi wa ku Samariya kuti anali Mesiya amene Mulungu analonjeza kupyolera mwa aneneri.

MTSOGOLERI:

Yesu anaphunzitsa ophunzira ace ndipo ali kuphunzitsabe masiku ano mnjira yomwe anakhalamo. Amaphunzitsa kupyolera mzinthu zomwe anacita. Yesu anaphunzitsa ophunzira ace ndipo anawatumiza kukhala mboni zace. Coyamba anatumizidwa kwa anthu awo ndiponso kwa anthu onse.

anati, "Sicabwino kutenga mkate wa ana ndi kuuponera tiagaru." Mkazi uja anabvomekeza za ici, koma anaonjezera mau nati, ngakhale tiagaru timadya nyenyeswa zakugwa pagome pa ambuye ao. Pamene Yesu anaona cikhulupiliro cace cacikuru, anapatsa mkaziyo comwe anali kupempha. Mwana wace anacilitsidwa.

GAWO LACIWIRI: YESU NDI KENTURIYO WA KU AROMA MATEYU 8.5-13

Yesu anali mu Kapernao pamene msilikali wa ci Roma anabwera nafunsa Yesu kuti apite kunyumba yace ndi kuciritsa mnyamata wace amene anali kudwala kwambiri. Pamene Yesu anabvomera kuti apite naye kunyumba yace, msilikali anati, "Sindiyenera kuti mukalowe pansi pa cindwi langa iai. Koma mungonena mau, ndipo adzaciritsidwa mnyamata wanga."

Yesu anadabwa pa za cikhulupiliro comwe anali naco. Yesu analankhula ku khamu la anthu nati Ahelene ambiri monga msilikali uyu wa ci Roma adzabwera kucokera mdziko lonse lapansi nadzalowa mu ufumu wakumwamba nadzakhala ndi Abrahamu, Isake ndi Yakobo.

GAWO LACITATU: YESU NDI MKAZI WAKU SAMARIYA (YOHANE 4.4-42)

Pamene Yesu anayenda kupyolera mu Samariya nalankhula kwa Msamariya pa citsime, anali atauza ophunzira ace kuti anafuna kupita kupyolera mu Samariya. Mkazi wa ku Samariya ndi ophunzira a Yesu anadabwa kwambiri pa zomwe Yesu anacita. Yesu anaswa malamulo ambiri a Ayuda pamene analankhula ndi mkazi wa ku Samariya.



ndipo anacilitsidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Pamene anacilitsidwa anati, "Tsopano ndidziwa kuti kulibe Mulungu wina mdziko lonse." Naamani analonjeza kuti sankapembedza mafano kapena Mulungu wina wonama.

MTSOGOLERI:

Buku la Masalmo ndi buku lomwe linasonkhanitsa nyimbo zomwe zinayimbidwa pakupembedza Mulungu. Colinga ca Mulungu cakubweretsa munthu kwa iye cinali phunziro la Masalmo ambiri. Masalmo 67 ndi kuitana kwa Ayuda kutenga Mulungu ku mitundu yonse ya anthu a mdziko lapansi. Ayuda sanakhoze kuika Uthenga uwu mmitima yawo ndi mzocita zawo. Motero kuti, Cipangano Cakale ciri ndi nkhani zing'ono za anthu ena amene anakhala ali kupembedza Mulungu. Koma m'miyoyc ya anthu awa, colinga ca Mulungu cinacitika.

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: COLINGA CA MULUNGU CINABVUMBULUTSIDWA KWA ANENERI

MAU A MULUNGU: Yesaya 11.1-10

MAU APAMTIMA: *"Pakuti dziko lapansi lidzadzazidwa ndi cidziwitso ca ulemerero wa Yehova, monga madzi aphimba pansi pa nyanja."*
*Habakuku 2.14*

MTSOGOLERI:

Aneneri a Mcipangano Cakale analankhula kwa ana a Israyeli pa za cimo m'miyoyo ya anthu. Aneneri anaitana anthu kuti atembenuke. Amos anali mneneri amene analankhula za cilungamo ca Mulungu ndi kudzudzula zoipa zomwe zinali m'miyoyo ya ana a Israyeli.

Aneneri mu Uthenga wao anakumbutsanso ana a Israyeli colinga ca Mulungu comwe anali naco powasankha iwo. Hoseya amaonetsa cikondi ca Mulungu kwa anthu onse a mdziko lapansi. Malembedwe a aneneri amanena za ciweruzo ca Mulungu comwe cidzabwera pa ana a Israyeli cifukwa cakukana kwao kuuza anthu ena za Mulungu mmodzi wamoyo yekha.

GAWO LOYAMBA: YESAYA

Ulaliki wa Yesaya umanena za kubwera kwa Mesiya ndi m'mene colinga ca Mulungu





COLINGA CAMIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: YESU NDI AHELENE

MAU A MULUNGU: Yohane 12.20-32

MAU APAMTIMA: *"Pakuti kulibe kusiyana Myuda ndi Mhelene; pakuti Yemweyo ali Ambuye wa onse, nawacitira zolemera onse amene aitana pa Iye; pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka."*
*Aroma 10.12-13*

MTSOGOLERI:

Yesu analalikira kwambiri ku ana a Israyeli. Ophunzira ace anatumizidwa coyamba ku ana a Israyeli. Unali mpata wao wosilizira kuti akwanilitse mbali ya lonjezo lawo. Buku Lopatulika litiuza mmalo ambiri zomwe zinacitika pamene Yesu anakomana ndi anthu ena amene sanali Ayuda.

GAWO LOYAMBA: YESU NDI MKAZI WA KU FONIKE

Mu Mateyu 15.22-28 Yesu analankhula kwa mkazi amene anafuna Yesu kuti aciritse mwana wace. Yesu anayesa cikhulupiliro cace pakusaikako nzeru ku copempha cace. Ophunzira ace anapempha Yesu kuti amucotse cifukwa kupempha kwace kunali kuwakalipitsa. Tsono Yesu anayesa cikhulupiliro ca mkaziyo pakunena kuti cipulumutso cinali ca Ayuda. Pamene mkazi anabweranso napempha, Yesu

lalikuru naitana anthu ambiri. Pa nthawi ya phwando mwini wa phwando anatuma kapolo wace kuti abweretse iwo akuitanidwawo. Oitanidwawo anapanga zifukwa zina nakana kubwera kuphwando. Pamene mwini phwando anamvera za ici, anakalipa anauza kapolo wace kuti apite ku njira za mudzi ndi kubweretsa aumphawi ndi opunduka ndi akhungu ndi otsimphina. Pamene mwini phwando anamva kuti kunali malo opanda anthu, anatumanso kapolo wace kupita kukafuna funa anthu amene ankapezeka kuti abwere motero kuti nyumba yace idzale ndi anthu. Ndipo mwini nyumba anati, "Kulibe mmodzi wa amuna oitanidwa aja adzalawa phwando langa."

Mnthanoyi mwini phwando ndi Mulungu ndipo oitanidwa ndi Ayuda.

MTSOGOLERI:

Acipembedzo ambiri anali osakhulupilira kuti Yesu anali Mesiya. Anali kuyembekezera Mesiya amene ankamasula dziko lawo kucokera mu ulamulilo wa a Aroma. Anakana kumvera zomwe Yesu anali kuwauza. Pamene Yesu anawadzudzula kamba ka kusakhulupilira kwao, atsogoleri a ci Yuda anayamba kufuna funa njira yakupheramo Yesu Kristu.



cidzakwanilitsidwa. Malembedwe a Yesaya amalankhula za zinthuzi kupambana aneneri ena. Yesaya anaoenjezanso anthu a Israyeli. Mulungu anazibvumbulutsa yekha kwa ana a Israyeli moyenera kupambana mitundu ina ya anthu. Cifukwa ca ici anthu a Israyeli ankaweruzidwa kopambana mitundu ina ya anthu.

Yesaya anakumbutsanso anthu a Mulungu kuti anayenera kukhala mboni ku dziko kuletsa kupembedza mafano ndi kukhala nyali kwa Ahelene. Aneneri onse anadziwa kuti Yehova anali Mulungu wa anthu onse. M'buku la Yesaya 66, Yesaya ali kuona mloto nthawi yomwe anthu onse adzapembedza Mulungu.

GAWO LACIWIRI: YONA

Mulungu anaitana Yona kuti akalalike ku Ninive. Pamene Yona anayesa kuthawa Mulungu, anaphunzira kuti Yehova anali Mulungu wa anthu onse a mdziko lapansi. Yona sanali okondwa pa kuona kuti anthu a mu Ninive anatembenuke ndi kuyamba kupembedza Mulungu.

Yona anaimilira ana a Israyeli. Ana a Israyeli anakumbutsidwa za colinga comwe Mulungu anali naco pa iwo. Sanakondwe ndi pangano la Mulungu. Sanafune kuti Mulungu adalitse anthu a mitundu ina ya mdziko lapansi. Anakalipa pamene anaona anthu ena kuti anatembenuka ndi kupeza ciyanjano ndi Mulungu.

GAWO LACITATU: MALAKI

Malaki anali mneneri wosilizira amene Mulungu anaitana kuti acenjeze anthu ace osankhidwa. Malaki anakhala kwa zaka 400 pomwe Yesu Kristu asanabadwe. M'buku la

Malaki tiuzidwanso kuti anthu osankhidwa ace a Mulungu ali akukalipitsa iye. Ana a Israyeli sanamvetsetse za colinga ca Mulungu pa kuwagwiritsa nchito ya kutsogolera Ahelene kuti akhulupilire Mulungu.

Mu Malaki 1.10-11 muli cenjezo la mphamvu kwa ana a Israyeli lakuti atembenuke kapena adzaona ciweruzo ca Mulungu pa iwo monga anthu. Malaki ali kucenjeza kuti Mulungu adzasankhanso wina kuti akwanilitse colinga cace cifukwa colinga ca Mulungu cakubweretsa munthu kwa iye ciyenera kucitidwa.

MTSOGOLERI:

Cipangano Cakale cinatha ndi cenjezo ndi kuitana kukutembenuka kwa ana a Israyeli. Ciri cacisoni kuti zaka zambiri zapitazo kucokera pomwe lonjezo linapangidwa kwa Abrahamu ndi pa nthawi ya utsogoleri wa Mose, ana a Israyeli sanamvetsetse kapena kukwanilitsa colinga ca Mulungu m'miyoyo ya mitundu ya anthu. Patapita zaka 400 Mulungu yekha mwa Yesu adzabweretsa kuitana kosilizira pa za kutembenuka.



wa ku dziko lina amene Ayuda samfuna amenenso atha kuthandiza munthu wopwetekedwa. Yesu analankhula za kupita ndi kukhala ngati Msamariya wacifundo Yesu anati muyenera kuonetsa kuti mutsatira malamulo a Mulungu pa zomwe mucita osati mzomwe mukhulupilira cabe.

GAWO LACIWIRI: LUKA 15.3-32

Mu Luka 15 Yesu ali kunena za nthano zomwe zimaonetsa cikondi kwa iwo amene ali kutali ndi iye. Nthano ya ndalama yotaika, nkhosa yotaika ndi mwana wolowelera zitiuza kuti Mulungu, amafuna funa iwo anthu amene sadziwa iye. Mulungu ali kufuna funa iwo amene ali otaika ndipo kumakhala cikondwelero cacikuru pamene wotaika apezeka.

Mnthano ya mwana wolowelera, tate ndi Mulungu. Mwana wamkuru ayimilira mmalo a ana a Israyeli. Mwana wamkuru ali wacisoni kamba kakuti mwana wolowelera abwereranso ku nyumba. Safuna kuti agawirane naye madalitso a atate. Safuna kuti agawane ndi m'bale wace amene anali kukhala mu cimo kutali ndi Mulungu. Mulungu ali okondwa kuona kuti mwana wolowelera abwera kunyumba. Mulungu akumbutsa mwana wamkuru kuti anali ndi madalitso a atate ace kwa nthawi zonse. Mulungu afunsa mwana wa mkuru kuti abwere pafupi ndi kukondwera pamodzi kamba kakuti mwana wolowelera wabwera kunyumba.

GAWO LACITATU: LUKA 14.16-24

Mu Luka 14 Yesu Kristu ali kunena za nthano ya munthu amene anakonza phwando

MUTU 7

COLINGA CA MIYEZI ITATU: **KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA**

COLINGA CA LERO: **YESU NDI AYUDA**

MAU A MULUNGU: **Luka 4.16-30**

MAU APAMTIMA: *"Pakuti Kristu ali cimariziro ca lamulo kulinga kucilungamo kwa amene ali yense akhulupira."*
*Aroma 10.4*

MTSOGOLERI:

Yesu anayamba kulalikira ndi kutuma ophunzira ace kwa ana a Israyeli. Ana a Israyeli anapatsidwanso mpata wosilizira kuti atembenukile kwa Mulungu, kukhulupilira Mulungu, ndi kumvera iye ndi kukwanilitsa lonjezo. Poyamba Yesu anadabwa cifukwa sanakhulupilire iye. Mwamsanga anadziwa bwino kulimba kwa mitima yawo. Ankaona mmene ana a Israyeli anadela Mulungu ngakhale mmaganizo akuti iwo okha anali opembedza oona a Mulungu.

GAWO LOYAMBA: LUKA 10.25-37

Mu Luka 10 Yesu alankhula za nthano ya Msamariya wacifundo. Yesu anati lamulo la Mulungu liri kuti tikonde mnansi wathu monga mmene tizikondela ife eni. Nthano ya Msamariya wacifundo itiuza kuti munthu aliyense amene ali kufuna thandizo ndi mnansi wathu! Mnthanoyi anthu a cipembezo alephera kuthandiza munthu wa dziko lawo. Ndi munthu



MUTU 6

COLINGA CA MIYEZI ITATU: KUFALITSIDWA KWA UTHENGA WA M'BUKU LOPATULIKA

COLINGA CA LERO: YESU ALI KUKWANILITSA LONJEZO LA MULUNGU

MAU A MULUNGU: Yeremiya 31.31-34

MAU APAMTIMA: *"Taonani, masiku adza, ati Yehova, ndipo ndidzapangana pangano latsopano ndi nyumba ya Israyeli, ndi nyumba ya Yuda."*
*Yeremiya 31.31*

MTSOGOLERI:

Pamene Yesu Kristu anabadwa, lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu linakwanilitsidwa. Mulungu analonjeza Abrahamu kuti kupyolera ku kholo lace dziko lonse lidzadalitsidwa. Luka ndi Mateyu amapereka maina amene amaonetsa Yesu kuti acokera ku kholo la Abrahamu. Pamene Yesu anabadwa, angelo anauza azibusa kuti Yesu adzabweretsa mtendere pa dziko lapansi ndi kwa anthu onse.

GAWO LOYAMBA: LONJEZO LAKALE

Ana a Israyeli analephera kugawira ena Uthenga wa Mulungu ndi dziko monga Mulungu anafunila iwo kuti acite. Mulungu anali wodekha mtima ndi ana a Israyeli. Anali ndi mipata yambiri yakuuza dziko za cikondi cace ndi kuthandiza munthu kuti akhale mciyanjano ndi Mulungu. Tsopano Mulungu anali kugwiritsa nchito munthu mmodzi wocokera ku kholo la

Abrahamu kudalitsa dziko lonse.

Moyo wa Yesu ndi moyo wa mwana wa Mulungu pakati pa anthu ace. Mu moyo wa Yesu, Mulungu anaonjezera kapena kupitiriza cikondi cace ku mitundu ina osati ana a Israyeli okha ai.

GAWO LACIWIRI: LONJEZO LA TSOPANO

Pamene Mulungu anatuma Mwana wace mdziko lapansi, anapanga lonjezo latsopano ndi anthu atsopano. A Israyeli sanalinso anthu osankhidwa ace a Mulungu. Anthu osankhidwa ace a Mulungu ankakhala iwo amene ankalandila Yesu Kristu monga Mpulumutsi ndi kuyamba kuyenda mciyanjano ndi Mulungu.

Ana a lonjezo latsopano anali kuyenera kukhala ndi malamulo a Mulungu ali olembedwa mu mitima yawo. "....Ndipo kuti, ana a thupi sakhala iwo ana a Mulungu ai; koma ana a lonjezo awerengedwa mbeu yace." (Aroma 9.8).

GAWO LACITATU: YESU, MPULUMUTSI WA DZIKO

M'buku la Mateyu 13, Yesu Kristu ali kufanizira ufumu wa Mulungu monga kambeu ka mpiru ndi cotupitsa mkhate. Mu Uthenga wa ciphunzitso ca pa phiri mu Mateyu 5, Yesu auza ophunzira ace kuti ali ngati mcere wa dziko ndi kuunika. Mau awa aonetsa momwe ufumu wa Mulungu uliri kufalitsidwa mdziko lonse. Ciyambi cidzakhala mwa pang'ono koma uthenga udzapitabe malo onse ndi kumveka mdziko lonse lapansi. Uthenga wa Yesu Kristu uyenera kukhala kuunika mu mdima mu dziko lapansi.



Nchito ya Yesu Kristu muno mdziko lapansi inacitika kwa zaka zitatu cabe. Mzakazo Yesu anaphunzitsa guru laling'ono la ophunzira kuti afalitse Uthenga Wabwino wa Mulungu kwa anthu onse a mdziko lapansi.

MTSOGOLERI:

Lonjezo lakale kwa ana a Israyeli linasamila pa kumvera lamulo lomwe linapatsidwa kupyolera mwa Mose. Malamulo khumi analembedwa pa miyala. Lonjezo la Mulungu latsopano linali lakuti lamulo la Mulungu linkalembedwa mmitima ya anthu ace. Ankalemba malamulo ace mumitima yawo. Pamene Yesu abwera mu mtima wa munthu ndi mmoyo wace, lonjezo latsopano la Mulungu limakwanilitsidwa.